

1. a. Mayinawa adachokera ku ziyankhulo zotsatirazi:

- i. kachasu: Chipwitikizi
- ii. thaulo: Chingerezi
- iii. ndege: Chiswahili
- iv. gomo: Chishona

- b. i. pophatikiza mphatikiram'mbuyo 'wam-' ku tsinde lenileni lamfotokozi '-kazi'
- ii. pophatikiza mphatikiram'mbuyo 'za-' ku dzina "chitsulo"
- iii. pophatikiza mphatikiram'mbuyo 'to-'ku mneni 'fewa'

2. a i. Anyamata akusewera mpira.

ii. Makedzana anthu amavala zikopa.

iii. Iye tidzakhala titafika pamene inu muzidzanyamuka.

b.

- i. mgwirizanitsi waubale
- ii. mgwirizanitsi wamchitantchito
- iii. mgwirizanitsi waumwini
- iv. mgwirizanitsi woloza

3. a. i. iye wati sabwera kuno.

ii. Abambo atimenya tiana tija.

iii. Tinsomba tanu tawola.

b. i. kukhala mchitidwantchito

ii. kusonyeza malo

iii. kusonyeza kudandaula

iv kukamba za dzina 'munthuyo'



4. Mariya: dzina

lamwinimwini

mchitantchito,

chimodzi

chachikazi

gulu la Mu-, A-

wabwera: mneni,

wosayambukira

kanenedwe kofotokoza

nthawi yatsopano yathayi

dzulo: muonjezi, wanthawi

GAWO B (MALIKISI 20)

Kumvetsa nkhani ndi kusanthula chiyankhulo

a. i. Sekwa

ii. Anthu ake samadziwa kulima

Milandu nayo imawavuta kuweruza

iii. Amakonda kuseketsa anthu akamacheza

iv. Damalisi adachenjezedwa kuti akaulula aphedwa.

v. Adanyazitsa mafumu a m'mudzi ponena kuti mfumu ndi nduna zake zidalibe luso
loweruzira milandu

vi. Adamukonzera chiwembu choti wapha nkhoa ya mfumu.

vii. Sadachite bwino chifukwa chinthu chikalakwika chimafunika kukonza.

b. i. atizolowera/atiderera

achilape

zitsiru



sitichenjera

- ii. - Anthu pachibale amakumana kuseri n'kukwanitsa kukupanga chipongwe
-Ngakhale mkamwini atapeza zitsiru pamudzi sakuyenera kumaderera anthu.

GAWO C (Malikisi 15)

Chifupikitso

Ndevuzamwayi

Pali ena amaganiza/ kuti ndalama sizingapezeke/ popanda mankhwala.
/Ndevuzamwayi adaganizanso chimodzimodzi./

Iye adapita kwa sing'anga/ yemwe adawauza/ kuti akaphe mwana wachisamba./
Adaphadi nalemera./

Posakhutitsidwa adapitanso/ nakatenga mankhwala obero/ ndipo chizimba n'kukhala
ziwalo za wachibale. /

Adalemera nagula katundu wambiri./ Anthu adazindikira/ choncho adamangidwa./
Chumanso chidatha./

GAWO D (Malikisi 15)

Chimasuliro

Kukhala ndi mtendere wamtima

Moyo wamtendere ukutanthauza kuyamba tsiku lililonse ndi kukhutira komanso chimwemwe.
Kukhala pa mtendere anthu amaona kuti ndi moyo wathanzi. Mtendere wa mtima nthawi zambiri
zimagwirizana ndi kukhala ndi chimwemwe.

Maganizo abwino, kuphatikiza ndi ntchito zabwino, kumalenga zotsatira zabwino. Mbali inayi,
maganizo oyipa, kuphatikiza ndi ntchito zoyipa, zimachititsa kudandaula, kuwawidwa komanso
kuvutika. Ngati munthu alibe mtendere, munthu angathe kupanga ziganizo zomwe zingachotse



moyo. Kusweka mtima ndi moyo wa nkhawa ndi adani a mtendere. Achinyamata a mu Malawi akulimbikitsidwa kupewa kusweka ndi kupsinjika mu mtima kuti akhale moyo wodzadzidwa ndi mtendere.

